

## CHIYEMBEKEZO CHODALA

Mawu a Mulungu akutiiza pa **Tito 2v13** kuti: *“akulindilira chiyembekezo chodala ndi maonekedwe a ulemelero wa Mulungu wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu.”* Tsopano ndikufuna ndikambe za chiyembekezo chimenechi.

Choyambilira, chiyembekezo sichinthu choti tingachigwire m'manja mwathu, koma ndi chinthu chomwe tingachigwire mu mtima mwathu. Chiyembekezo chathu ndichakuti tsiku lina tidzasiyana nalo dziko lino la uchimo, ndikukakhala muyaya kumwamba, pamaso pa Mulungu. Tikadzafika kumwamba tikudziwa kuti sikudzakhala imfa kapena kulira, kulibe kumva zowawa, kulibe njala, kulibe misozi, koma chikondi, mtendere ndi chimwemwe. (**Chibvumbulutso 21v4**). Tidzakhala ndi Mulungu kwa muyaya. Sitidzakhanso ndi thupi la uchimo lomwe ndi lofooka koma tidzasinthika kukhala anthu auzimu ndikukhala nalo thupi ngati la Yesu (**Afilipi 3v21**). Ndizovuta kuti timvetsetse kutanthauza kokhala ndi matupi a uzimu, koma mawu a Mulungu akutiiza kuti tidzasinthika. Kotero, tikuyenera kukhala ndi chitsimikizo kuti izi zidzachitika ndipo tidzamvetsetsa nthawi imeneyo. Chomwe tikudziwa ndichakuti kumwamba sitidzanzuzikanso mu njira ina iri yonse, kudzakhala kwa ngwiro monga Mulungu ali wa ngwiro, ndipo ichi ndicho chiyembekezo chopambana chomwe tikuyenera kuchigwiritsitsa.

Chiyembekezo ndi chikhulupiliro ndizolumikizana ndipo timakhala ndi chiyembekezo chifukwa cha chikhulupiliro chathu. Pa **Aheberi 11v1** tikuuzidwa kuti: *“koma chikhulupiliro ndicho chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka, chiyesero cha zinthu zosapenyeka”* Sitingathe kuchiona chikhulupiliro koma kudzera mu chikhulupiliro, timakhala ndi chiyembekezo chodzakhala ndi Yesu tsiku lina. Pa vesi lomwe tawerenga poyambilira lija, tikuuzidwa kuti Yesu, chiyembekezo chathu chodala, adzabweranso pa dziko lino lapansi tsiku lina. Vesi linanso likutiiza kuti, pamene Iye adzabweranso, adzabweretsa chipulumutso kwa iwo omwe akuyembekezera Iye (**Aheberi 9v28**). Choncho ngati tikhalabe ndi moyo, tidzamuona Iye pamene adzabweranso ndipo pamene adzabweranso, adzatenga onse okhulupilira kukakhala naye kwa Mulungu. Ngati timwalira Iye asanabwere, tidzaukitsidwa ku moyo wosatha, ndipo tonse tidzakomana naye mlengalenga. Choncho chiyembekezo chathu ndikuona Yesu tsiku lina komanso kukhala naye mpaka muyaya. Chiyembekezo ichi sichinthu choti tingachione, koma chinthu chomwe tingachisunge mkati mwa mtima mwathu komanso kuchiyembekezera.

Baibulo likutipatsa zitsanzo za anthu achikhulupiliro chachikulu komanso chiyembekezo. Yobu anali m'modzi wa iwo. Yobu anakhalapo zaka mazana Yesu asanabwere, ndipo anayesedwa ndi satana koma anasunga chikhulupiliro. Anali ndi chuma chochuluka, ana amuna asanu ndi awiri, komanso ana akazi atatu, koma anataya zonsezi pamene Mulungu analola satana kuti amuyese. Anazunzika ndi zilonda, ananyozedwa ndi abwenzi ake koma sanataye chiyembekezo chake pa Mulungu. M'kati mwa zowawa zake izi, anati *“koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo, nadzauka potsiriza pafumbi.”* (**Yobu 19v25**). Ngakhale anazunzika sanalole zochitika za padziko kuononga chiyembekezo chake chakumwamba.

Paulo anali munthu winanso wa chikhulupiliro chachikulu komanso chiyembekezo mwa Yesu. Nthawi zambiri anazunzika pamene anatenga uthenga pa dziko lapansi. Anali mundende, anakwapulidwa kasanu ndi chikwapu, anamenyedwa ndi ndodo katatu,

anagendedwa miyala kamodzi komanso anazunzika munjira zina zambiri. Koma m'malo moti chikhulupiliro ndi chiyembekezo chake zionongeke, mayesero amenewa anamulimbikitsa ndipo anati: "... *ndisefukira nacho chimwemwe m'chisautso chathu chonse.*" Paulo ndi chitsanzo kwa ife cha munthu amene anazunzika chifukwa cha Yesu ndi Uthenga koma osataya chiyembekezo. **Aroma 12v12** akulankhula kwa inu ndi ine kuti "*kondwerani m'chiyembekezo.*"

Pali amayi ndi abambo achuluka omwe amaima nji atakomana ndi mazunzo. Tikawerenge **Aheberi 11**, tipeza zitsanzo za anthu a chikhulupiliro komanso chiyembekezo cha moyo wosatha kumwamba. Buku limeneli limatchedwanso kuti 'Buku la Amuna a Chikhulupiliro.' Likulankhula za anthu ngati Nowa, Abrahamu komanso ena ochuluka amene anaphedwa, kuikidwa mu ndende, kuzunzidwa, kugendedwa miyala, kukwapulidwa ndi zina zotero. Koma onsewa sanachoke pamaso pa Mulungu, anakakamira ku chikhulupiliro chawo komanso chiyembekezo cha chiukitso chopambana.

Tsopano tiyeni tione zinthu zomwe inu ndi ine tikuyenera kuchita kuti chikhulupiliro ndi chiyembekezo chathu chikule pamene tikuyembekezera kubwera kwa Yesu Khristu. Tikaona amuna achikhulupiliro a pa **Aheberi 11**, tikuona kuti chikhulupiliro chawo chinadza chifukwa cha kukhulupilira komanso kumvera. Sanadziwe zomwe Mulungu amayembekezera kwa iwo zokha ayi, komanso anamumvera Mulunguyo. Mwachitsanzo, Nowa anali wolungama komanso omvera Mulungu pomanga chombo. Popeza Nowa anakhulupilira ndi kumvera malamulo a Mulungu, anapulumutsidwa kuchigumula. Pamene munthu alemekeza komanso kumvera Mulungu, Mulungu amabwezera mphotho pobwera chifupi ndi iye komanso kuwapatsa chikhulupiliro chachikulu. Pali lonjezo lodabwitsa mu Baibulo lomwe likuti: "*Yandikirani kwa Mulungu ndipo adzayandikira kwa inu.*" **Yakobo 4v8**. Pamene Mulungu abwera chifupi ndi ife, tidzakhala ndi chidziwitso chachikulu cha kupezeka kwake ndipo izi zizakuza chikhulupiliro ndi chiyembekezo chathu pa Iye.

Abrahamu anamvera Mulungu, anakhala chifupi ndi Mulungu ndipo Mulungu anamutcha iye m'zake. Nanga inu ndi ine tikuyenera kuchita chani kuti Mulungu atitche anzake? Chachidziwikire ndichakuti ngati pali munthu yemwe sitilankhula naye, sizingatheke kuti akhale mzathu. Kutu Mulungu akhale mzathu, tikuyenera kulankhula naye pafupi pafupi, mpaka titadziwa njira zake. Ngati tikufuna kukhala chifupi ndi Mulungu, komanso kuti Iye akhale mzathu, tikuyenera kulankhula naye kudzera mu pamphero ndikuphunzira zokhudza Iye kudzera mu kuwerenga Baibulo. Tikachita izi tizamdziwa iye mwakuya ndikumvera malamulo ake chifukwa tizadziwa chomwe Iye amafuna.

Tikamvetsetsa vesi lotsatirali, tiona kuti Mulungu akutiiza kuti tifike chifupi ndi Iye mwa chikhulupiliro kugwiritsitsa chiyembekezo cholonjezedwa, kukhala m'chikondi kupitiliza kusonkhana pamodzi ngati mpingo. **Aheberi 10v22-25** akuti: "*tiyandikire ndi mtima woona, m'chikhulupiliro chokwanira ndi mitima yathu yowazidwa kuichotsera chikumbu mtima choipa, ndi matupi athu osambitsidwa ndi madzi oyeru; tigwiritse chibvomerezo chosagwendera cha chiyembekezo chathu, pakuti wolonjezayo ali wokhulupirika; ndipo tiganizirane wina ndi mzake kuti tifulumizane ku chikondano ndi ntchito zabwino, osaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amachita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku liri kuyandika.*"

Tsopano ndikufunsi funso, kodi muli ndi chikhulupiliro komanso chiyembekezo cholimba kapena anthu amakugwedezani msanga chikhulupiliro chanu? Ngati chikhupiliro ndi chiyembekezo chanu ndichosalimba, mukuyenera kufika chifupi ndi Mulungu posonkhana

ndi akhristu anzanu, kupemphera komanso kuwerenga Baibulo. Anzanu adzakuthandizani komanso kukulimbikitsani, koma ndi Mulungu yekha yemwe azakupatsani mphamvu. Pamene mupanga chisankho chofika chifupi ndi Mulungu, mudzaona kupezeka kwake mu moyo wanu chifukwa amatikonda ndipo amafuna kutidziwitsa kuti tikupanga zinthu zolondola. Kupeza nthawi yopemphera komanso yowerenga Baibulo zikhoza kukhala zovuta, koma tikamufunsa Mulungu kuti atithandize, izi zizatheka ndipo tizazichita.

Ndikufuna ndimalize ndi vesi lomwe likutiuzana kuti tilingalire zinthu zokhazo zomwe ziri zabwino kuti tisalore zinthu zapadziko lapansi kuononga chikhulupiliro komanso chiyembekezo chatu mwa Yesu. **Afilipi 4v8** akuti: “ *Chotsalira, abale, zinthu ziri zonse zoona, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyera, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma,; ngati kuli chokoma mtima china, kapena chitamando china, zilingilireni izi.*”

Yang'anani maso anu pa Yesu.

Contact: Pastor Sam D Phiri  
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671  
Email: [samdinala@yahoo.com](mailto:samdinala@yahoo.com)

Written by:  
Mick Alexander  
Email: [leeandmick@gmail.com](mailto:leeandmick@gmail.com)  
[www.ChristianIssues.biz](http://www.ChristianIssues.biz)